EXAMINATION NO.:___________________________

# PUTEYA ZONAL EXAMINATIONS BAORD

## 2021 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

**(100 marks)**

Thursday 8 July

Subject Number: P032

Time Allowed: 2hrs 15min

13:00 – 15:15am

Name of Candidate: ___________________________________________
(Surname First)

Name of School: ___________________________________________

## Instructions

1. **Pepala ili lili ndi masamba 9 chonde yang'anani.**
2. Lembani nambala yanu ya mayeso pa mwamba pa tsamba liri lonse
3. Pepala liri ndi magawo anayi, gawo A, B, c ndi D
4. Yankhani funso limodzi mu gawo A ndi mafunso onse m'magawo otsatirawo. Mugawo D, zunguzani lembo A, B, C kapena D.
5. Chongani nambala la funso limene mwayankha pa tebulo lomwe liri pa tsambali.
6. Tsatani malangizo a funso liri lonse.

**Zofunika**

- Chonde onetsetsani kuti mwalemba dzina lanu, nambala ya mayeso ndi dzina la sukulu yanu pa tsamba liri lonse.
- Perekani pepala lanu la mayeso kwa oyang'anira mayesowa pakutha kwa nthawi.

| | **Tick 41-51 If answered** | **Do not write in these columns** | |
|---|---|---|---|
| 1 - 20 | | | |
| 21 - 40 | | | |
| 41 | | | |
| 42 | | | |
| 43 | | | |
| 44 | | | |
| 45 | | | |
| 46 | | | |
| 47 | | | |
| 48 | | | |
| 49 | | | |
| 50 | | | |
| 51 | | | |
| | | | |

© 2021 Puteya Zone

**GAWO A (30 Malikisi)**

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri omwe ali mmusiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata.

Mawu a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma isabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu ULENDO OSAIWALIKA.

Mwa zina tsatani izi polemba.

**Ndime yoyamba**
**.** Kodi udali ulendo opita kuti?
. Kudachitika zotani?
. Nanga zidachitikitra malo otchedwa chiyani?

**Ndime yachiwiri**
. Momwe ulendowo udakukhuzirani
. Mudatengapo mbali yanji pa zochitikazo

**Ndime yachitatu**
. Zinthu zomwe zidachititsa kuti ulendowo ukhale osaiwarika

**KAPENA**

2. Yerekezani kuti mwasankhidwa kukayamba form1 ku Namisale Sekondale sukulu koma simupita nsanga chifukwa chakuti mukudwala. Lembani kalata kwa mphunzitsi wamkulu wa Namisalle Sekondale Sukulu, P.O.Box 70, Befu yomudziwitsa (kuti) zakudwala kwanu

Mwa zina tsatani izi poleba kalata yanu.

**Ndime yoyamba**
. Cholinga cha kalata
. ndinu mnyamata kapena msungwana
. komwe munkaphunzira

**Ndime yachiwiri**
. Matenda omwe mukudwala
. nthawi yomwe mudayamba kudwala matendawa
. Zomwe mukuchita kuti muchire
. Mukuyembekeza kufika liti ku sukuluko

**Ndime ya chitatu**
. Zomwe mudzachite mukapita ku sukuluko kusonyeza kuti mwayamba mochedwa

© 2021 Puteya Zone 

EXAMINATION NO.:____________________________

© 2021 Puteya Zone

GAWO B (20 Malikisi)

3. Werengani nkhani yotsatilayi mosamala kwambiri kenako yakhani mafunso otsatilawo.

**PA BWALO LA MILANDU**

Pabwalo pamakhala kanenedwe kake ka milandu kamene kamatchedwa chowa. Chowachi chimachitika pofuna kuona bwino magwelo ake a milandu. Popeza kalelo padalibe mchitidwe omalemba pamene oyankhula ali kufotoza. Oweluza adali kubwerezanso mawu aja amene munthu wanena.tsono uja ofotoka amabuula kuti mmm! Mmm!kuvomereza kuti obwereza mawu aja adali kulongosola molondola.

Pabwalo loweluzira miandu lotchedwa cha kwanu leka, mmawa tsiku loweluka dzuwa litangotuluka pang'ono, anthu adali kudikira a mfumu bwana Issa kuti ayambe kuweluza milandu. Mwadzidzi anthu adaona mfumuyi ndi akulu a bwalo, a Muholo ndi Alandasi akutulukira kuti bala manthu. Anthu onse adangoti gwadu gwadu. Mmenemo nkuti sekulu pa mtima pake pali thi thi thi mfumu Bwana Isa adali ndi chikaliwo wake chiri ndi utsi kuti phwa, phwa, phwa masinya ali khwe, khwe, khwe ngati ayambana ndi munthu.

Ehe!adayankhula mfumu bwana isa akukhala pa chitsa cha mtengo. Nthawiyo akulu abwalo nkuti atakhala kale pansi. "Chete!" adatelo mkulu wa bwalo Landasi. Tsopano mverani mfumu bwana Isa. "pano monga mudziwa," adatelo mfumu Bwana Isa. "Ndi pa Chakwanu leka pamene mboni zikuperekera umboni sindifuna kumadzidula mawu. Pamene wina ali kufotokoza nkhani mmene idayendera musamaikire mangombe. Pomaliza nkhani iri yonse ndidzagamula molingana ndi umboni ndi kakhalidwe ka nkhani."

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere iri pansi pa funso lililonse.

A. Kodi chowa ndi chiyani? **(2 malikisi)**

___________________________________________________________

___________________________________________________________

___________________________________________________________

B. Kodi cholinga chochitira chowa nchiyani? **(2 malikisi)**

___________________________________________________________

___________________________________________________________

___________________________________________________________

C. Chifukwa chiyani oweluza milandu kale adali kubwerezanso zomwe anthu anena. **(2 malikisi)**

___________________________________________________________

___________________________________________________________

___________________________________________________________

D. Fotokozani chifukwa chomwe ofotokoza milandu amabuulira **(2 malikisi)**

E. Perekani mutu wa mawu awa mu nkhaniyi **(2 malikisi)**

i. Chete!

ii. Bwalo.

F. Kodi mawu oti 'akulu a bwalo' atanthauzanji **(2 malikisi)**

G. Perekani mivekelo iwiri kuchokera mu nkhani iyi **(2 malikisi)**

H. "Chete! Tsopano mverani mawu a mfumu." Adanena mawu amenewa ndani **(2 malikisi)**

I. Kodi mawu oti "kuikira man'gombe" akutanthauzanji? **(2 malikisi)**

J. Perekani malo omwe nkhaniyi inachitikira **(2 malikisi)**

**Gawo C (10 malikisi)**

Yankhani mafunso onse weiri mgawoli.

4. Werengani ka nkhanika ndipo myankhe mafunso otsatirawa.
"Ndichifukwa chiyani mwagwira tambala pakamwa chonchi? Odwala uja kapena wabzyala chinangwa? Pepani thambo lagwa."

**Mafunso**

.a. Ndimalonje anji akuperekedwa kankhanika **(1 malikisi)**

© 2021 Puteya Zone 

b. Ndani akuyankhula kankhanika **(1 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

**c.** Perekani mawu ofanana mmatanthauzo oti bzyala chinangwa **(1 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

B. Tchukani udindo wa munthu yemwe amayankhula ka nkhanika **(1 mailikisi)**

______________________________________________

C. Perekani vuto limodzi kuipa kumodzi kwa mankhwla ozunguza bongo.

**(1 malikisi)**

______________________________________________

______________________________________________

5. **Kupanga ziganizo**
   Panagni ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa **(5 malikisi)**

   Mawango: ______________________________________________

   Tho: ______________________________________________

   Konza: ______________________________________________

   Uja: ______________________________________________

   Phweka: ______________________________________________

## GAWO D (40 malikisi)

Zunguzani lembo lokhonza (A, B, C kapena D) ma funso otsatilawa.

Mafunso **6** mpakana **10**, sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mnzere kunsi kwawo mu zoganizo zotsatirazi.

6. Eneya <u>wachila</u> nthenda ija
   A. Dzina
   B. mneni
   C. mperekezi
   D. muonjezi

7. Ndatenga <u>awiri</u> okha
   A. Mlowammalo
   B. Dzina
   C. Mperekezi
   D. Mfotokozi

8. Ndiri ndi mwana <u>wa mfupi</u>
   A. Mneni
   B. Muonjezi
   C. Mlowammalo
   D. Mfotokozi

9. <u>N</u>'kale lija tidaonana
   A. Mneni
   B. Nfotokozi
   C. Mperekezi
   D. Muonjezi

10. Mulungu akhale <u>ndi</u> inu
    A. Dzina
    B. Mperekezi
    C. Mlowammalo
    D. Muonjezi

Mafunso 11 mpaka 14. Sankhani magulu a maina omwe atsekedwa mnere kusni kwawo.

11. Joni waphika <u>nyemba</u>
    A. Ka -, Ti
    B. I -, Zi
    C. Chi -, Zi
    D. Mu -, A

12. <u>Munthu</u> akubwerayo ndamudziwa
    A. I -, Zi
    B. Mu -, Mi
    C. Ku -, Pa-, Mu
    D. Mu -, A

13. Khasu ndalisiya <u>mmunda</u>
    A. Ku -, Pa-, Mu
    B. Ka -, Ti
    C. Chi -, Zi
    D. I -, Zi

14. <u>Gulu</u> limodzi lokha silokwanira
    A. U -, Ma
    B. Mu -, Mi
    C. Li -, Ma
    D. I -, Zi

Mafunso 15 mpaka 17. Sankhani miyambi yomwe ikutsutsana ndi miyambi yomwe yakembedwa mmusimu.

15. Mwala oyenda yenda suyanga ndele.
    A. Wakwatira kwa phenzi saopa kung'anima
    B. Patsala paja pagona chinziri
    C. Pamodzi pamodzi padaoletsa dzungu
    D. Kalikokha nkanyama

16. Muvi oyang'anira suchedwa kulowa mmaso
    A. Ali dele nkulinga utayenda naye
    B. Kuona maso a nkhono nkudekha
    C. Mapanga awiri avumbwitsa
    D. Chala chimodzi sichiswa nsabwe

17. Kanthu nkhama pwhiti adakwatira njiwa
    A. Fupa lokakamiza silichedwa kuswa mphika
    B. Kuona maso a nkhono nkudekha
    C. Mwana wang'ona sakulira dziwe limodzi
    D. Kambalame kolawilira kadakhuta ndi nyongolosi.

Mafunso 18 paka 19. Sankhani mikuluwiko yofanana mmatanthauzo ndi yomwe iri mmusimu.

18. Galu wa mkota sakandira pachabe
    A. Mutu umodzi susenza denga
    B. Utsi siufuka popanda moto
    C. Kutsutsa galu nkukumba
    D. Anyani kusekana zikundu

19. Kanthu nkavumbu kadavumbula mende pachitsa
    A. Fodya wako ndi uyo ali pa mphuno
    B. Khoswe wapa tsindwi adaulula wa pa dzala
    C. Chikondi cha bulangete
    D. Fodya mpa nazale

© 2021 Puteya Zone 

Mafunso 20 mpaka 23. Sankhani mawu otsutsana mmatanthauzo ndi omwe adulidwa mnzere kunsi kwao mu ziganizo zotsatirazi.

20. Nkhuzi ija yalowa mkhola
    A. Nsoti
    B. Ntheno
    C. Mnthoni
    D. Tambala

21. Muphwa wanga wabwera
    A. Mfumukazi
    B. Mdzakazi
    C. Mkazi
    D. Mfumukozi

22. Gojo amakhala mokhumata
    A. Mkazi
    B. Ntheno
    C. Chumba
    D. Mzizi

23. Mtchembele ya mmudzi muno yadwala
    A. Mphulu
    B. Muna
    C. Ndoda
    D. Kapolo

Mafunso 24 mpaka 26. Sankhani ntchito za 'ndi' zoyenera mmunsimu (kukhala).

24. Joni ndi mnyamata wabwino
    A. Dzina
    B. Mfotokozi
    C. Muonjezi
    D. Mneni

25. Joni ndi Mina abwera
    A. Mneni
    B. Mfotokozi
    C. Mlumikizi
    D. Mlowammalo

26. Benita wamenyadwa ndi ndodo
    A. Mlumikizi
    B. Mperekezi
    C. Muonjezi
    D. Mfotokozi

Mafunso 27 mpaka 31. Sankhani nthawi za aneni oyenera omwe atsekedwa mnzere kunsi kwawo

27. Ndimachoka posachepa
    A. Yakale
    B. Yakale yathayi
    C. Yatsopano yathayi
    D. Yakale yopitilira

28. Dani adalowa ntchio chaka chatha
    A. Yakale yathayi
    B. Yakale
    C. Yakale yopitilira
    D. Yatsopano yathayi

29. Ndinkaphunzitsa kuno chaka cha 2014
    A. Yakale yakawiri kawiri
    B. Yakale yopitilira
    C. Yakale
    D. Yakale yathayi

30. Ndidyabe ndikamva njala
    A. Yatsopano
    B. Yatsogolo yopitilira
    C. Yatsogolo
    D. Yobwerezabwereza

31. Tizidzavina naye usiku
    A. Yamtsogoo yakawirikawiri
    B. Ya mtsogolo yopitilira
    C. Yamtsogolo
    D. Yatsopano

Mafunso 32 mpaka 34. Sankhani chachimuna cha zinthu zaerekedwazi

32. Azakhali
    A. Amai
    B. Achemwali
    C. Amalume
    D. Achimwene

33. Nsoti
    A. Nkota
    B. Tambala
    C. Thazi
    D. Mphongo

34. Namwali
    A. Mnyamata
    B. Mtsikana
    C. Amai
    D. Agogo

Mafunso 35 mpaka 38. Sankhani Chichewa choyenera cha mawu omwe atsekedwa mnzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi

35. Mnyamata ndimam’basopa ndine
    A. Ndimansunga
    B. Ndimamusamala
    C. Ndinamubala
    D. Ndimamukonda

36. Mina pita ku sinje
    A. Ku tsinje
    B. Ku mtsinje
    C. Ku msinje
    D. Ku musinje

37. Anthu ambiri chaka chino amanga manyumba
    A. Zinyumba
    B. Zimanyumba
    C. Nyumba
    D. Timanyumba

38. Iwe usiye kutentha Makala
    A. Kuyatsa
    B. Kuotcha
    C. Kuwotcha
    D. Kuosha

Funso 39 mpaka 41. Sankhani mawu omwe akutsiriza ntchezelo zotsatirazi.

39. Kulimba mtima ngati___________
    A. Ovuula mchenga
    B. Ofula agalu
    C. Olemera
    D. Ocheka matabwa

40. Mantha ngati ______________
    A. Wakuba
    B. Mwana
    C. Fisi
    D. Mkango

41. Kuda ngati
    A. Makala
    B. Galu
    C. Munthu
    D. Mdima

Mafunso 42 mpaka 45. Sankhani nthambi za chiganizo yosaima payokha yomwe yatsekedwa mnzere kunsi kwawo.

42. Iye walandira kalata yoti akalandilire ndalama.
    A. Ya dzina
    B. Ya neni
    C. Ya mfotokozi
    D. Ya muonjezi
43. Mwnaayo amayenda ngati akudwala
    A. Ya mfotokozi
    B. Ya muonjezi
    C. Ya dzina
    D. Ya mneni
44. Dolesi wavala dilesi lomwe adamugulira atsibweni ake.
    A. YA mfotokozi
    B. Ya muonjezi
    C. Ya dzina
    D. Ya mneni
45. Sindiziwa chomwe ndidalakwa
    A. Ya mneni
    B. Ya mfotkozi
    C. Ya muonjezi
    D. Ya dzina

**MAFUNSO ATHERA PANO**

© 2021 Puteya Zone